PHUNZIRO LA 16

1. Kodi Kayini ndi zidzukula zake amkakhulupilira chiyani?
-Kayini ndi zidzukulu zake amkakhulupilira kumangosangalala ndi ndalama ndi zinthu zimene anali nazo.

2. Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, kodi Satana anamuletsa Mulungu kuti achite zimene amkafuna kuchita.
-Iyayi.

-Palibe amene angamuletse Mulungu kuchita zimene wafuna kuti azichite.

3. Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, kodi Mulungu analiyiŵala lonjezo Lake lotumiza Mpulumutsi?
-Iyayi.

-Mulungu sayiwala malonjezo lake.

4. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamupatsa Adamu ndi Hava mwana wina dzina lake Seti?
-Chifukwa chakuti Kayini anamupha Abele, Mulungu anakhoza zotumiza Mpulumutsi kupitila mu mtundu wa Seti.

5. Kodi chifukwa chiyani Adamu ndi Hava anafa?
-Chifukwa chakuti Adamu ndi Hava sanamumvere Mulungu ndipo anamumvera Satana.

6. Kodi chifukwa chiyani anthu onse amafa?
-Chifukwa cha machimo awo.

7. Kodi chilango cha Mulungu pa tchimo ndi chiyani?
-Imfa.

8. Kodi Enoki amkadziwa chiyani za iye?

-Enoki amkadziwa kuti anabadwa ali mwana wa Adamu ndi Hava.
-Enoki amkadziwa kuti anabadwira kunja kwa munda wa Edeni.
-Enoki amkadziwa kuti anabadwira mu tchimo.
-Enoki amkadziwa kuti anabadwira mu imfa.

9. Kodi Enoki amkadziwa chiyani za Mulungu?
-Enoki amkadziwa zakuti Mulungu ndi oyera.
-Enoki amkadziwa kuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Enoki amkadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene anali oyenera kumupulumutsa iye.
-Enoki amkakhulupilira kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzaŵapulumutsa anthu kwa Satana.

10. Kodi chinachitika ndi chiyani chimene chinali chodabwitsa kwa Enoki?
-Mulungu anamutenga Enoki ndikupita naye kumwamba kukakhala ndi Iye.

11. Kodi kumwamba ndi kotani?
-Kumwamba ndi ku malo okongola kwambiri kumene kulibe kudandawula kapena kulira, kulibe matenda kapena imfa.

12. Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamutenga Enoki ndikupita naye kmwamba?
-Chifukwa chakuti Enoki amkamumvera Mulungu.
-Chifukwa chakuti Enoki anapita kwa Mulungu mu njira ya Mulungu yekha.

-Pamene Mulungu anamutenga Enoki kupita naye kumwamba, panapita zaka zambiri, ndipo anthu ambiri anabadwa pa dziko la pasi.



Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:22

22-Chomcho Nowa anapanga zonse zimene Mulungu anamulamula.

-Nowa anamukhulupilira Mulungu.
-Nowa anakhulupilira kuti Mulungu sanama.
-Nowa anakhulupilira kuti Mulungu atumiza chigumula cha madzi ngati m’mene ananenera Iye.

-Chomcho, Nowa anapanga chombo ngati m’mene Mulungu analamulila.

-Ngakhale kuti Nowa anali asanayiwone mvura chiyambire, iye anakhulupilira kuti Mulungu atumiza chigumulacho.

-Pamene Nowa amkapanga chombocho, iye amkawawuza anthu kuti adzimumvera Mulungu.
-Pamene Nowa amkapanga chombocho, iye amkawawuza anthu kuti adzimvera mwa Mulungu.

-Pamene Nowa amkapanga chombocho, iye amkawawuza anthu kuti Mulungu adzatumiza chigumula cha madzi kuti chidzawononge dziko la pasi.

-Nowa amkawawuza anthu za Mulungu ngati m’mene ndikukuwuzirani ine za Mulungu.

-Kodi mukuganiza zakuti anthu amkamumvera Nowa?
-Timva mu phunziro likudzali.

-Kodi Mulungu amkafuna kuti Nowa apange bwanji chom-
bo?
-Ngati m'mene anamulamulilira Mulungu.

-Mulungu amkafuna kuti Nowa apange chombo ngati m'mene anamulamulilira Mulungu.

-Mulungu amkafuna kuti Nowa apange chombo mu njira ya Mulungu yekha.

-Zovala za Adamu ndi Hava zimkayenera kuti zipangidwe mu njira ya Mulungu yekha.

-Kodi Mulungu anamulamula Nowa kuti apange zombo zingati?
-Chombo chimodzi.

-Panali chombo chimodzi chokha chimene Nowa akanapulumukira.
-Panalibe chombo china chilichonse chimene Nowa anakapulumukira.

-Kodi Mulungu anamulamula Nowa kuti apange makomo angati za chombocho?
-Khomo limodzi.

-Panali khomo limodzi lokha limene Nowa anakaloŵera mchombo muja kuti apulumuke.
-Panalibe njira ina yiliyonse yimene Nowa anakaloŵera mchombo muja kuti apulumuke.

-Kodi mukuganiza kuti Nowa anamumvera Mulungu?



-Ndipamene zidzukulu za Seti ndi Enoki zinapitiriza kumumvera Mulungu, koma anthu ambiri amkamumvera Satana.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:1-2

1-Pamene anthu anayamba kuchuluka pa dziko la pansi, ana ambiri achikazi anabadwa,
2-ana achimuna a Mulungu anawona kuti ana achikazi a anthu osakhulupilira anali akongola, ndipo anayamba kukwatira amene amkamukonda.

-Kodi ana achimuna a Mulungu anali ndani?
-Anali ana a mu mtundu wa Seti.
-Anali ana achimuna amene amkakhulupilira mwa Mulungu.

-Kodi ana achikazi a anthu anali ndani?
-Ana ana a mu mtundu wa Kayini.
-Anali akazi amene samkakhulupilira mwa Mulungu.

-Kodi ana achimuna a mu mtunda wa Seti amkachita chiyani kwa ana achikazi a mu mtundu wa Kayini?

-Ana achimuna  a mu mtundu wa Seti anayamba kukwatira ana achikazi a mu mtundu wa Kayini.

-Amuna amene amkakhulupilira mwa Mulungu anayamba kukwatira akazi amene samkakhulupilira mwa Mulungu.

-Kodi chinachitika ndi chiyani ana achimuna a mu mtundu wa Seti atayamba kukwatira ana achikazi a mu mtundu wa Kayini?

-Anthu ambiri samkafuna kumumvera Mulungu.
-Anthu ambiri amkamumvera Satana yekha.

-Anthu ambiri samkatsatsa njira ya Mulungu.
-Anthu ambiri amkatsata njira yawo.

-Kodi mukuganiza kuti Mulungu anali osangalala pamene anthu ambiri samkafuna kuti adzimumvera Iye.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:3

3-Tsopano Ambuye Mulungu anati, "Sindidzalola anthu kukhala ndi moyo mpaka kalekale, popeza kuti munthu, ndi thupi limene limafa. Kuyambira tsopano adzingokhala ndi moyo kwa zaka 120.

-Mulungu sanali osangalala pamene anthu ambiri samkafuna kumumvera Iye.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu amafuna kuti anthu adzimumvera?
-Kuti anthu asadzawonongedwe.

-Chomcho, Mulungu anati kuti adziyankhulana ndi anthu kwa zaka 120 zokha.

-Kodi ngati anthu anakapitirizabe kutsatira njira zawo, Mulungu anakachita chiyani kwa iwowo?

-Mulungu anakaŵalanga ndi imfa.

-Kodi Mulungu amkalankhula bwanji kwa anthu?

-Mulungu Mzimu Woyera amkalankhula m'maganizo mwawo.



Uchipange mosanjikiza, chikhale cha nyumba zitatu, ndipo m'mbali mwake mukhale chitseko.

17-Ndidzagwetsa mvura ya chigumula pa dziko la pasi, kuti iwononge za moyo zonse. Zonse za pa dziko zidzafa,

18-koma iweyo ndidzachita nawe chipangano.Udzalowe mchombomo pamodzi ndi mkazi wako, ndi ana ako amuna pamodzi ndi akazi awo.

19-Ndipo udzatengenso nyama za mtundu uliwonse, yayimuna ndi yayikazi, kuti zisungidwe ndi moyo.

20-Mbalame za mtundu uliwonse ndi nyama zazikulu ndi zokwawa zomwe, zidzalowe mchombomo ziŵiriziŵiri, yayimuna ndi yayikazi, kuti zisungidwe ndi moyo.

21-Udzatengenso zakudya za mtundu uliwonse kuti inu ndi nyamazo mudzidzadya."

-Mulungu anamulamula Nowa kuti apange chombo pa mulingo weniweni wa mulitali umene Mulungu analamula.

-Mulungu anamulamula Nowa kuti apange chombo pa mulingo weniweni wa mchifupi umene Mulungu analamula.

-Mulungu anamulamula Nowa kuti apange chombo pa mulingo weniweni wa msinkhu umene Mulungu analamula.

-Kodi Mulungu amkafuna kuti Nowa apange chombo mu njira yake ya Nowayo?
-Iyayi.

-Mulungu samkafuna kuti Nowa apange chombo mu njira yake ya Nowayo.

-Chifukwa chakuti Nowa amkakhulupilira mwa Mulungu, Mulungu anaganiza zomupulumutsa Nowa, ndipo Mulungu anamulamula Nowa.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:13-14

13-Chomcho Mulungu anati kwa Nowa, “Ine ndiŵawononga anthu onse, chifukwa chakuti dziko la pasi ladzadza ndi zochita zawo zonyansa. Ndatsimikiza kuti ndiliwononga dziko la pasi pamodzi ndi iwowo.
14-Iwe uzipangire chombo ndi matabwa ochokera ku mitengo ya mnjale. Ukhoze zipinda mkati mwake, ndipo uchimate ndi phula mkati ndi kunja komwe.”

-Kodi Nowa anamulamula chiyani Nowa?
-Mulungu anamulamula Nowa kuti apange chombo.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu anamulamula Nowa kuti apange chombo?
-Chifukwa chakuti Mulungu amkafuna kutumiza chigumula cha madzi kudzaŵawononga za moyo zonse za pa dziko la pasi.

-Mulungu anamupatsa Nowa malamulo ambiri okhuza kapangidwe ka chombocho.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:15-21

15-[Mulungu anati kwa Nowa] “Umu ndi m’mene upangire chombocho: Mlitali mwake mwa chombocho mukhale mamita 133. Mu lifupi mwake mukhale mamita 22, ndipo msinkhu wake ukhale wa mamita 13.
16-Upange denga la chombocho, ndipo usiye mpata wa masentimita 44 pakati pa dengalo ndi m’mbali mwake.



-Kodi Mulungu Mzimu Woyera amkalankhula chiyani kwa anthu?

-Mulungu Mzimu Woyera ankawawuza anthu kuti adzimvera kwa Mulungu osakhala kwa Satana.

-Mulungu Mzimu Woyera ankawawuzanso anthu kuti adzitsatira njira ya Mulungu yekha asakhala njira yawo.

-Kodi Satana nayenso amalankhula ndi anthu kupitira m’maganizo awo?
-Inde.

-Kodi Satana amawawuza chiyani anthu?

-Satana amawawuza anthu kuti asamamumvere Mulungu.

-Kodi chifukwa chiyani Satana safuna kuti anthu azimumvera Mulungu?

-Satana amafuna kuti wina aliyense asamumvere Mulungu kuti adzawonongedwe.

-Ngati mukukana kuti Mulungu adzilankhula kwa inu kupitira m’maganizo anu, Mulungu adzakulangani.

-Kodi ndi kwabwino kumumvera Mulungu kusiyana ndi Satana?

-Ngakhale kuti Mulungu Mzimu Woyera amalankhula kwa anthu, kodi anthu amamvera?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:11

11 Koma anthu ena onse anali oyipa pa maso pa Mulungu, ndipo kuyipa kwawo kunafarikira ponseponse.

-Ngakhale kuti Mulungu Mzimu Woyera amkalankhula kwa anthu, anthu ambiri amkakana kumvera kwa Mulungu.

-Ndipo dziko la pansi linadzadza ndi chisokonezo.

-Tamverani zimene anthu amkachita:

-Anali ozikonda.
-Anali awumbombo.

-Amkaŵachitira msanje anthu ena.
-Amkaŵadyera masuku pa mutu anthu ena.

-Amkawanamiza anthu ena.
-Amkalankhula zoyipa za anthu ena.
-Amkaŵada anthu ena.

-Anali oyipa.
-Anali achisokonezo.

-Amkamenyana ndi anthu ena.
-Amkaŵapha anthu ambiri.

-Samkayifuna njira ya Mulungu.
-Amkangofuna njira yawo yokha.

-Kodi anthu a masiku ano ndi ofanana ndi anthu a m'masiku a Nowa?
-Inde.

-Kodi anthu a masiku ano ndi ozikonda ndipo a umbombo?



-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti Mulungu amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.
-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti Mulungu yekha ndi amene angathe kumupulumutsa iye.

-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti Mulungu adzatumiza Mpulumutsi kudzamupulumutsa iye ku machimo ake.

-Chifukwa cha chikondi cha Mulungu, Mulunguyo anaganiza zosamuwononga Nowa.

-Kodi chikondi ndi chiyani?

-Apa pali chitsanzo:

-Nthaŵi zambiri wakuba amkamubera munthu oyandikirana naye, ndipo wakubayo amkadziwika.
-Tsiku lina, wakubayo anatitimira m'madzi wosefukira.
-Wakubayo anatsala pang'ono kumila.
-Koma munthu oyandikirana naye uja anamuwona wakubayo akumira ndipo anakamupulumutsa.

-Ngakhale kuti wakubayo amamubera munthu woyandikirala nayeyo nthaŵi zambiri, iye anamupulumutsa wakubayo.

-Ngakhale kuti wakubayo amayenera kumira, munthu woyandikirana naye uja anamupulumutsa iye.

-Ichi ndiye chikondi.

-Umu ndi m'mene Mulungu amatipulumutsira ife tikamamukhulupilira Iye.

9-Nayi mbiri ya Nowa. Nowa anali munthu wochita zokondweretsa Mulungu, wopanda cholakwa, ndipo pa nthaŵi imeneyo anali yekhayo amene amayenda ndi Mulungu.
10-Nowa anali ndi ana atatu: Semi, Hami, ndi Yafeti.

-Kodi chifukwa chiyani Mulungu sanaganize zomuwononga Nowa?
-Kodi chifukwa chakuti Nowa sanachimweko?
-Iyayi.

-Nowa anabadwa ali ochimwa ngati anthu onse.
-Nowa anabadwa ali kapolo wa Satana ngati anthu onse.

-Kodi nanga chifukwa chiyani Mulungu anaganiza zosamuwononga Nowa?

-Chifukwa chakuti Nowa sanamumvere Satana.
-Chifukwa chakuti Nowa anamumvera Mulungu.

-Chifukwa chakuti Nowa sanatsatire njira yake.
-Chifukwa chakuti Nowa anatsatira njira ya Mlungu yekha.

-Chifukwa chakuti Nowa amkadikira Mpulumutsi.

-Chifukwa chiyaninso Mulungu anaganiza zomupulumutsa Nowa?

-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti anabadwira mu uchimo.

-Chifukwa chakuti Nowa anadziwa kuti wamuchimwira Mulungu.



-Inde.

-Kodi anthu a masiku ano amaŵanamiza anthu ena ndiponso kunena zoyipa za iwowo?
-Inde.

-Kodi anthu a masiku ano amaŵamenya anthu ena ndikumaŵapha iwowo?
-Inde.

-Kodi anthu a masiku ano amafuna njira yawo osakhala njira ya Mulungu?
-Inde.

-Anthu amenewo anabadwa ali ochimwa chifukwa chakuti anali zidzukulu za Adamu ndi Hava.

-Anthu tonse tinabadwa tili ochimwa chifukwa chakuti tili zidzukulu za Adamu ndi Hava.

-Kodi Mulungu akuŵawona machimo awowo?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:5,12

5-Mulungu anawona kuti zochita za anthu a pa dziko la pasi ndizoyipa kwambiri, ndiponso kuti mitima yawo ndi yodzadza ndi maganizo oyipa nthaŵi zonse.
12-Mulungu anawona kuti dziko la pasi lanyansa kwambiri, chifukwa chakuti anthu onse anali oyipa kwambiri.

-Inde, Mulungu anaŵawona machimo onse.

-Mulungu amaliwona tchimo lililonse.

-Palibe amene angathe kubisa tchimo lake lina lililonse kwa Mulungu, chifukwa chakuti Mulungu ali paliponse.

-Mulungu amaliwona tchimo lililonse, ndipo amapereka chilango pa tchimo lililonse.
-Mulungu amaliwona tchimo, lililonse ndpo amapereka chilango pa tchimo lililonse ndi imfa.

-Kodi Mulungu anaganiza chiyani atawona kuti anthu onse akuchimwa?

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:6-7

6-Ambuye Mulungu anadandawula chifukwa chakuti anaŵalenga anthu ndikuŵayika pa dziko la pasi, ndi zimenezi, anaŵawidwa mtima kwambiri.
7-Chomcho Mulungu anati, "Anthu onse amene ndinaŵalenga pa dziko la pasi lino ndiŵawononga. Ndiwononganso nyama zonse ndi zokwawa zomwe, pamodzi ndi mbalame zomwe, pakuti ndikumva chisoni kuti ndinazilenga."

-Mulungu anali okwiya chifukwa cha machimo a anthu onse.

-Chifukwa chakuti dziko la pasi linadzadza ndi machimo a anthu, Mulungu anaganiza zoŵawononga anthu onse.

-Chifukwa chakuti dziko la pasi linadzadza ndi machimo a anthu, Mulungu anaganiza zowononga za moyo zonse za pa dziko la pansi.

-Kodi mukuganiza kuti Mulungu amkangolankhula chabe?
-Kodi kapena mukuganiza kuti Mulungu adzazichita zimene analankhula kuti adzazichitazo?



-Mulungu anamuwuza Adamu ndi Hava kuti adzafa ndipo adzasiyana ndi Mulungu akadzadya chipatso chimene Mulungu anaŵaletsa kudya.

-Kodi Mulungu amkangolankhula chabe, kapena Mulungu anazichita zimene analankhula kuti adzazichitazo?
-Mulungu anazichita zimene analankhula kuti adzazichitazo.

-Mulungu anamuwuza Kayini ndi Abele kuti apite kwa Mulunguyo mu njira ya Iye yekha, ngati sakutero adzakanidwa.

-Kodi Mulungu amkangolankhula chabe kapena anachita zimene analankhula kuti adzazichitazo?
-Mulungu anazichita zimene analankhula kuti adzazichita.

-Mulungu sali ngati anthu.
-Anthu amatha kunena kuti achita chinthu china chake koma osachichita chinthucho.

-Mulungu sali ngati anthu.
-Mulungu nthaŵi zonse amachita zimene walankhula kuti adzazichita.

-Chifukwa cha chikondi ndi chisoni cha Mulungu, panali munthu m'modzi amene Mulungu sanafune kuti amuwononge.

Tiyeni tiŵerenge Genesesi 6:8-10

8-Koma Nowa yekha ndi amene anali wangwiro pa maso pa Mulungu.